PHUNZIRO LA 63

1. Kodi chifukwa chiyani ophunzira a Yesu anaŵadzudzula anthu chifukwa chopita ndi ana awo kwa Yesu kuti akaŵakhudze?
-Ophunzira a Yesu ankaganiza kuti Yesu sankafuna kuti adzivutitsidwa ndi ana.

2. Kodi Yesu amaŵakonda ana onse?
-Inde.

3. Kodi ana nawonso akufunika kuti apulumutsidwe ku mphamvu ya tchimo, imfa ndi Satana?
-Inde.

4. Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani pamene analankhula kuti aliyense amene sawulandila Ufumu wa Mulungu ngati mwana, sadzaloŵa mu ufumuwo?
-Yesu ankatanthawuza kuti ngati sitikukhulupilira mwa Mulungu ndi chikhulupiliro ngati cha mwana, siti-dzapulumutsidwa.

5. Kodi chikhulupiliro ngati cha mwana ndi chotani?
-Chikhulupiliro cha mwana chimakhala chenicheni.
-Chikhulupiliro cha mwana chimakhala cha mtima onse.

6. Kodi funso limene mnyamata wa chuma anamufunsa Yesu linali lotani?
-"Kodi ndiyenera kuchita chiyani kuti ndilandire moyo osatha?

7. Kodi Yesu anayankha chiyani?
-Yesu anayankha kuti, "Kodi chifukwa chiyani ukunditcha Ine wabwino? Palibe wabwino, koma m'modzi yekha – ndiye Mulungu.

8. Kodi Yesu ankakana kuti Iye sanali wabwino?
-Ayi.

9. Kodi Yesu ankakana kuti Iye sanali Mulungu?
-Ayi.

10. Kodi nanga chifukwa chiyani Yesu analankhula zimene analankhulazo?
-Yesu ankafuna kuti munthu uja amvetsetse kuti chifukwa chakuti anthu onse anabadwira mu tchimo, palibe munthu wabwino.
-Yesu ankafuna kuti munthu uja amvetsetse kuti chifukwa chakuti Mulungu yekha ndi amene alibe tchimo, Iye ndiye wabwino.

11. Kodi mnyamata wa chuma uja ankaganiza kuti angawupeze bwanji moyo osatha?
-Pochita ntchito zabwino.

12. Kodi chimene sanamvetsetse munthu uja ndi chiyani?
-Munthu uja sanamvetsetse zakuti ntchito zathu zabwino zimene timachita panja, sizingathe kusintha mitima yathu yoyipa imene ili mkati.

13. Kodi chifukwa chiyani mnyamata wa chuma uja anapita kwawo ali asakondwa?
-Chifukwa chakuti sankafuna kuti apereke chuma chake chonse kwa osawuka.
-Chifukwa chakuti sankafuna kuti Yesu awusinthe mtima wache woyipa uja.

14. Kodi ndi ndani yekha amene angathe kutipulumutsa ife ku mitima yathu yoyipa?
-Yesu Kilisitu.

-Yesu Kilisitu yekha ndi amene angathe kutipulumutsa ife



Tiyeni tiŵerenge Luka 16:30

30-Koma iye anati kwa iye, “Iyayi, Atate Aburahamu, komatu wina akapita kwa iwo kuchokera kwa akufa adzatembenuka mtima.”

-Munthu wachumayo anati kuti, ngati munthu wina apite kuchokera kwa akufa ndikukaŵachenjeza abale ache, iwo angatembenuke mitima.

-Kodi nanga Aburahamu anayankha chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Luka 16:31

31-[Aburahamu] anati kwa iye, “Ngati samvera Mose ndi aneneri, sadzakopeka mtima ngakhale wina awuke kwa akufa.”

-Kodi Aburahamu anati chiyani kwa munthu wachumayo?
-Aburahamu anati kuti ngati abale akewo saŵamvera Mawu a Mulungu, ngakhale wina atabwera kuchokera kwa akufa , sadzakhulupilirabe.

-Ngati ife sitimvera Mawu a Mulungu ndikukhulupilira, pangakhalenso china chake chakuti chingatipulumutse ife?
-Palibe.

-Ilo ndi bodza la Satana.

-Munthu wachuma uja ankafuna kuti Lazaro akalankhule kwa abale ache kuti iwowo asadzavutike ngati m'mene ankavutikira iye ku malo amoto ndi chilango chosatha.

-Kodi nanga Aburahamu anamuyankhanso chiyani munthu wachumayo?

Tiyeni tiŵerenge Luka 16:29

29-Aburahamu anayankha kuti, "Ali ndi Mose ndi aneneri; aŵamvere iwowo."

-Aburahamu anamuyankha munthu wachumayo kuti abale akewo ali ndi Mose ndi aneneri amene ayenera kuŵamvera.

-Kodi Aburahamu ankatanthawuza chiyani atalankhula kuti abale akewo anali ndi Mose ndi aneneri?
-Aburahamu ankatanthawuza kuti abale a munthu wachumayo anali ndi Mawu a Mulungu amene analembedwa kudzera mwa Mose ndi aneneri.

-Kodi Aburahamu ankamuwuza munthu wachuma uja kuti abale akewo ayenera kuchita chiyani?
-Ankaŵawuza kuti iwo ayenera kuŵerenga ndi kumvera Buku la Mulungu, Bayibulo.

-Ngati tikuŵerenga ndi kumvera Mawu a Mulungu ndi kukhulupilira, ndiye kuti sitidzapita ku gahena, ku malo a moto ndi chilango chosatha.

-Kodi kenako munthu wachuma uja anayankhanso chiyani?



ku mitima yathu yoyipa.

-Chifukwa chakuti Yesu amayidziŵa mitima ya anthu onse, Iye anaŵaphunzitsa anthu za kusilira.

Tiyeni tiŵerenge Luka 12:15

15-Ndipo Iye anati kwa iwo, "Samalirani, ndipo chinjerani ndi kusilira: pakuti moyo wa munthu siwulingana ndi zinthu zimene iye ali nazo."

-Kodi chifukwa chiyani anthu amasilira?
-Chifukwa chakuti anthu onse anabadwira mu tchimo.
-Chifukwa chakuti anthu amafuna zinthu zimene alibe.

-Anthu ambiri amafuna chuma kuposa china chilichonse pa dziko la pansi pano.
-Anthu ambiri amafuna chuma kuposa Mulungu.

-Anthu ambiri amati akachiwona chuma cha anthu ena, iwowo amafuna kuti chikhale chawo.
-Anthu ambiri amaganiza kuti adzakhala osangalala akadzakhala ndi chuma chambiri.

-Kodi nanga ngati munthu ali ndi chuma pa dziko la pansi panno, chumacho chikamuthandiza iye akadzapita ku chilango chosatha?
-Ayi.

-Kodi miyoyo yathu ili ndi zinthu zambiri ?
-Ayi.

-Kodi zinthu zingathe kutipulumutsa ife ku tchimo, imfa ndi Satana.
-Ayi.

-Pofuna kuŵathandiza anthu kuti amvetsetse, Yesu anaŵawuza iwo fanizo.

Tiyeni tiŵerenge Luka 12:16-19

16-Ndipo [Yesu] anaŵawuza iwo fanizo ili: "Munda wa munthu wina wache wa chuma unabereka zokolora zambiri.
17-Kenako iye anaganiza mwa iye yekha, "Kodi ndidzachita chiyani? Ine ndilibe malo osungira zokolora zangazi."
18-Kenako iye anati, "Izi ndi zimene ine ndidzachite. Ndidzagwetsa nkhokwe zanga ndikumanga zazikulu, ndipo mu zimenezo ndidzasunga zokolora zanga ndi katundu wanga.
19-Ndipo kwa moyo wanga ndidzalankhula kuti, "Iwe moyo! Uli ndi katundu wambiri wabwino amene asungidwe kwa zaka zambiri. Chomcho masuka, idya, imwa, ndipo khala osangalala."

-Yesu analankhula fanizo la mulimi wachuma.

-Kwa chaka chatunthu, munda wa munthu wachuma unabereka zokolora zabwino ndipo zochuruka koma iye analibe nkhokwe zokwanira kusungira zokolorazo.

-Kodi kenako mwini munda wachuma uja anaganiza zochita chiyani?
-Iye anaganiza zomanga nkhokwe zazikuluzikulu zosungira zokolora zakezo pamodzi ndi katundu wache. Ndikumakhala mtima uli pansi m'moyo wache onse.

-Chifukwa chakuti mulimi ameneyu anali ndi chuma chambiri, iye ankaganiza kuti analibe vuto lina lililonse.

-Chifukwa chakuti mulimi ameneyu anali ndi chuma



-Ngati mukukana kumvera Mawu a Mulungu, mudzakhala ku malo a chilango mpaka kalekale.

-Kodi chachiŵiri chimene anapempha munthu wachuma uja kwa Aburahamu chinali chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Luka 16:27-28

27-Koma wachumayo anati, "Ndikukupempheni, Atate, mumutume Lazaro ku nyumba ya atate anga,
28-pakuti ndili ndi abale anga asano; akaŵachenjeze iwo kuti iwonso angadze ku malo ano a mazunzo.

-Kodi chifukwa chiyani munthu wachuma uja ankafuna kuti amutume Lazaro pa dziko la pansi?
-Munthu wachuma uja ankafuna kuti Lazaro akaŵachenjeze abale ache pa dziko la pansi.

-Ngakhale kuti munthu wachuma uja ankavutika kwambiri, iye ankaŵakumbukirabe abale ache .

-Kodi munthu wachuma uja anapempha chakudya kapena chofunda?
-Ayi.

-Kodi munthu wachuma uja anapempha magazi a nkhuku kapena mbuzi?
-Ayi.

-Satana ndi ziwanda zache wanamiza anthu ambiri.

-Anthu ambiri amaganiza kuti anthu akufa amafuna zofunda kapena chakudya kapenanso magazi a nkhuku ngakhale mbuzi.

Mpulumutsi.

-Munthu wachuma uja ankangodalira chuma chake chambiricho.

-Kodi anthu onse amene amakana kukhulupilira mwa Mulungu adzapita kuti akadzafa?
-Ku gehena, ku malo a moto ndi chilango chosatha.

-Kodi china ndi chiyani chimene analankhulanso Aburahamu kwa munthu wachuma uja?

Tiyeni tiŵerenge Luka 16:26

26-[Aburahamu anati] "Ndipo pamwamba pa zimenezi, pakati pa inu ndi ife pakhazikika phompho lalikuru kwambiri, kotero kuti iwo ofuna kuwoloka kuchokera kuno kunka kwa inu, sangathe, ngakhale kuchokera kwanuko ndikudza kwa ife, sangathenso."

-Aburahamu analankhulanso kuti, chifukwa chakuti panali phompho lalikuru kwambiri pakati pa kumwamba ndi gehena, panalibe amene anakatha kuwoloka.

-Kodi munthu amene adzaloŵe ku gahena adzathanso kuchokako?
-Ayi.

-Munthu akangoloŵa ku gahena, palibenso njira ina yopulumukira.

-Munthu akangofa ndikupita ku malo a chilango chosatha, adzakhala komweko mpaka kalekale.

-Ngati mukukana kumvera Mawu a Mulungu, mudzapita ku malo a chilango chosatha.



chambiri, iye ankaganiza kuti anali ndi china chilichonse.

-Chifukwa chakuti mulimi ameneyu anali ndi chuma chambiri, iye ankaganiza kuti ayiŵale za Mulungu, ndipo adzikhala malingana ndi njira zache.

-Ngakhale kuti mulimi wachumayu anamuyiŵala Mulungu, kodi nanga Mulungu anamuyiŵala iye?
-Ayi.

-Kodi kenako Yesu anati kuti chinachitika ndi chiyani kwa mulimi wachumayo?

Tiyeni tiŵerenge Luka 12:20

20-Koma Mulungu anati kwa iye, "Iwe opusa! Usiku wa lero moyo wako ndiwufuna. Nanga amene atenge zimene wazisungirazo ndi ndani?"

-Kodi chinachitika ndi chiyani kwa mulimi wachumayo?
-Mulungu anamuyitanira iye ku imfa.

-Kodi amene anasankha tsiku limene anamwalira mulimi wachuma uja anali ndani?
-Mulungu yekha.

-Kodi amene amasankha tsiku lofera munthu aliyense ndi ndani?
-Mulungu yekha.

-Kodi chinachitika ndi chiyani ku chuma cha mulimi wachuma uja?
-Anamusiyila munthu wina.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamutcha mulimi wachuma uja kuti ndi chitsiru?

-Chifukwa chakuti mulimi wachumayo ankaganiza kuti akhoza kumuyiŵala Mulungu ndikumakhala malingana ndi njira zache.

-Kodi chuma cha mulimi wachuma uja chinamupulumutsa iye?
-Ayi.

-Kodi mulimi wachuma uja anali ndi zinthu zonse?
-Ayi.

-Ngakhale kuti mulimi wachuma uja anali ndi chuma chambiri, kodi ankasoŵa chiyani?
-Moyo osatha.

-Kodi kenako Yesu analankhula chiyani atatha kulankhula fanizolo?

Tiyeni tiŵerenge Luka 12:21

21-“Umu ndi m’mene zidzakhalile kwa munthu amene akudzisungira yekha chuma koma ali opanda chuma pa maso pa Mulungu.”

-Yesu anati kuti, ngati ife tikuzisungira tokha zinthu zambiri, sikuti ife ndi achuma pamaso pa Mulungu, koma tidzakumana ndi imfa yosatha.

-Kodi chofunika kwambiri kuposa chuma chambiri ndi chiyani?
-Kukhulupilira mwa Mulungu ndikukhala ndi moyo osatha.

-Kenako Yesu anakamba nkhani yeniyeni.

Tiyeni tiŵerenge Luka 16:19-21



pa nthaŵi imene iye anali pa dziko la pansi pano, koma tsopano ndi nthaŵi yake yakuti asangalale.

-Kodi Lazaro anapita kumwamba chifukwa chakuti anali osawuka?
-Ayi.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Lazaro anapita kumwamba?
-Chifukwa chakuti anakhulupilira mwa Mulungu.

-Lazaro ankadziŵa kuti iye anabadwira mu tchimo.
-Lazaro ankadziŵa kuti Mulungu amapereka chilango cha imfa pa tchimo lililonse.

-Lazaro ankakhulupilira kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi kudzamupulumutsa iye.

-Kodi anthu onse amene amakhulupilira mwa Mulungu adzapita kuti akadzafa?
-Kukakhala ndi Mulungu kumwamba.

-Kodi munthu wachuma uja anapita ku moto chifukwa chakuti anali wachuma?
-Ayi.

-Kodi nanga chifukwa chiyani munthu wachuma uja anapita ku gahena?
-Chifukwa chakuti anakana kukhulupilira mwa Mulungu.

-Munthu wachuma uja sankakhulupilira kuti anabadwira mu tchimo.

-Munthu wachuma uja sankakhulupilira kuti Mulungu amapereka chilango cha imfa pa tchimo lina lililonse.

-Munthu wachuma uja sankakhulupilira kuti iye ankafuna

24-Ndipo [wachumayo] anakweza mawu nati, “Atate Aburahamu, mundichitire chifundo, mumutume Lazaroyo kuti aviike msonga ya chala chake m’madzi, nadzaziziritsa lilime langa, pakuti ndikuzunzikadi mu m’laŵi la motoli.”

-Kodi munthu wachuma uja, choyamba anamupempha Aburahamu kuti achite chiyani?
-Anamupempha Aburahamu kuti amutume Lazaro kuti aviike msonga ya chala chake m’madzi kuti akaziziritse lilime lache.

-Kodi chifukwa chiyani?
-Chifukwa chakuti munthu wachuma uja ankavutika kwambiri ku moto kuja.

-Anthu onse amene akukana kukhulupilira mwa Mulungu, adzafa ndipo adzapita ku moto, ku chilango chosatha.

-Mulungu amadana ndi tchimo, ndipo amapereka chilango cha imfa pa machimo onse.

-Kodi Aburahamu anayankha chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Luka 16:25

25-Koma Aburahamu anati, “Mwana, kumbukira kuti iwe unalandila zokoma zako uli ndi moyo, Lazaro akulandira zoyipa, koma tsopano iye akusangalatsidwa pano, iwe uli pa mavuto.

-Kodi Aburahamu anayankha chiyani?
-Aburahamu anayankha kuti munthu wachuma uja anali pabwino kwambiri pamene iye ankakhala pa dziko la pansi pano, koma tsopano ayenera kuvutika.

-Aburahamu ananenanso kuti Lazaro ankavutika kwambiri



19-[Yesu anati] “Panali munthu wina wache wa chuma, ankavala zovala za mtengo wapatali ndipo ankakhala moyo osangalala nthaŵi zonse.
20-Pakhomo pache panali munthu wina wache opemphapempha, odzala ndi zironda pa thupi lache, dzina lache Lazaro
21-ndipo ankafuna kukhuta ndi nyenyetswa zakugwa pa gome la mwini chumayo. Komatu ngakhale agalunso anadza kudzanyambita zironda zachezo.”

-Kodi tikudziŵa bwanji kuti nkhani imeneyi ndi yeniyeni?
-Chifukwa chakuti anthu aŵiri ameneŵa anakhalako pa dziko la pansi pano.

-Kodi anthu aŵiri ameneŵa ndi ndani mu nkhani imeneyi?
-Munthu wina anali wachuma wina osawuka.

-Kodi dzina la munthu osawukayu anali ndani?
-Lazaro.
-Uyu sanali Lazaro amene anali nzache wa Yesu amene anadzutsidwa ku imfa.

-Kodi amene anali odalitsika kwambiri mwa anthu aŵiriŵa ndi ndani?
-Kodi anali munthu wachuma amene ankavala zovala zapamwamba, ndikumadya chakudya chapamwamba, ndi amene anali odalitsika kwambiri?

-Kodi kapena Lazaro, amene anali osawuka ndipo wa zironda pa thupi lache, ndi amene anali odalitsika kwambiri?

-Mwina inu mukhoza kunena kuti amene anali odalitsika kwambiri ndi munthu wachuma uja, koma nkhaniyi siyinathe.

-Tamverani zimene analankhula Yesu za zimene zinachitika kwa anthu aŵiriwo.

Tiyeni tiŵerenge Luka 16:22

22-"Nthaŵi inafika imene munthu opemphayo adafa, ndipo angero anamutenga iye ndikupita naye ku chifuwa cha Aburahamu. Ndipo kenako munthu wa chumayo anafanso, nayikidwa m'manda.

-Kodi chinachitika ndi chiyani kwa munthu osawuka, Lazaro, atafa?
-Angero anamutenga ndikupita naye kumene kunali Aburahamu ndi Mulungu, kumwamba.

-Kodi nanga chinachitika ndi chiyani kwa munthu wachuma uja?
-Iye nayenso anafa.

-Kodi chuma cha munthu wachuma uja chinamuteteza ku imfa?
-Ayi.

-Kodi munthu wachuma uja anapita kuti atafa?

Tiyeni tiŵerenge Luka 16:23

23-Ndipo ku moto osatha (gehena) iye anakweza maso ache namuwona Aburahamu ali patali, ali ndi Lazaro ku chifuwa kwache.

-Kodi munthu wachuma uja anapita kuti atafa?

-Ku gahena, ku malo a moto ndi chilango chosatha.

-Munthu akafa, mzimu wache umapita kwa Mulungu, kumwamba, kapena ku gahena.



-Anthu ena amalankhula kuti munthu akafa, mzimu wache umayendayenda pa dziko la pansi pano.
-Ili ndi bodza lochokera kwa Satana.

-Anthu ena amanena kuti munthu akafa, mzimu wache umapita ku malo oyembekezera pakati pa dziko la pansi ndi kumwamba.
-Ilinso ndi bodza.

-Kodi pali malo ena oyembekezera pakati pa dziko la pansi ndi kumwamba?
-Ayi.

-Anthu ena amalankhula kuti amva mawu a makolo awo kapena munthu wina amene wafa kale.
-Ilinso ndi bodza lochokera kwa Satana.

-Mawu amene anthu amamvawo, amakhala ochokera kwa Satana ndi ziwanda zache.

-Munthu akafa, mzimu wache umapita kwa Mulungu, kumwamba, kapena ku gahena.

-Lazaro anafa ndipo mzimu wache unapita kukakhala ndi Mulungu kumwamba.

-Munthu wachuma uja nayenso anafa ndipo mzimu wache unapita ku malo a moto ndi chilango chosatha.

-Kodi munthu wachuma uja, choyamba anamupempha Aburahamu kuti achite chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Luka 16:24